KUKONDWERERA **CHIYERPO**

Mpingo wa Nazarene

CHICHEWA

06 January 2012

Okondedwa Abusa,

Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu Atate wathu ndi Ambuye Yesu Khristu zikhale ndi inu!

Ndikufuna kuonesa kuthokoza kwanga kwa inu chifukwa chakutenga nawo gawo mu utumiki osoza ndi kuphunzitsa anthu kuti akhale monga Yesu mu Chigawo cha Africa. Kuzipereka kwanu pa kulalikira Mawu a Mulungu, kupemphera, kusula oyera mtima pa ntchito ya utumiki, kusamalira anthu pa mpingo ndi ntchito zonse za utsogoleri ndi maudindo okhuzana ndi mautumiki zimene mumachita sabata ndi sabata ndi zoyamikilika kwambiri. Zikomo chifukwa cha ntchito zonse mumagwira.

Mpingo wa Nazarene mu Chigawo cha Africa ukupitilira kukula mu ntchito ndi chiwerengero cha anthu. Tinakondwerera kufika chiwerengero cha mamembala 500,000 chaka chatha mu maiko 42 mwa maiko 54 a mu chigawo cha Africa. Mulungu watidalitsa ndithu mmene tadziperekera pakumanga mpingo Wake muno mu Africa!

Pamene tikukondwerera kukula mu ntchito ndi chiwerengero cha anthu mu mpingo, ndikofunikira kuzikumbusa tokha cholinga chathu choyamba ngati mpingo, chimene chili kusunga ndi kufalitsa Chiyero cha Chikhristu monga chikupezekera mu Mawu a Mulungu, kudzera mukutembenuza mtima ochimwa, kudzutsa akugwa, ndi chiyeretso chathunthu kwa okhulupirira.

Pa kuona mtsogolo, Bungwe loyang'anira Utumiki ndi Bungwe Lalikulu la Alangizi mu Chigawo cha Africa anakomana mu mwezi wa September, 2011 kuganizira mfundo zimene zingalimbikitse kupitisa patsogolo chiyero kwa osatira Yesu, chiyero pofalitsa uthenga, kutsula utsogoleri, ndi kutukula mpingo. Anagwirizana ndi kuvomerezana pa mfundo yolimbikisa, "KUKONDWERERA CHIYERO", chaka cha 2012. Utumiki umenewu siukulowa mmalo mwa zimene inu mwakonza mu chaka cha 2012 ayi, koma kuthandizira ndi kulimbikisa ntchito yanu pa mpingo popitisa patsogolo moyo wa uzimu mu Chigawo cha Africa m'mene Mulungu Ali ndi ufulu kubweretsa chitsitsimutso mu mipingo yathu, ndi kuzutsanso miyoyo ya uzimu ya atsogoleri athu ndi mamembala athu. Tasankha ndi kukonza mabuku ndi makema oyenera pa utumiki umenewu amene tikukhulupilira kuti akuthandizeni inu kwambiri pamodzi ndi mpingo onse.

Utumiki umenewu udzayamba pa tsiku la Phulusa Lachitatu, 22 February 2012, ndi nthawi ndi mapemphero, kusala kudya, kusanthula Mawu ndi kuonetsetsa mozama kulowa mu Pasaka Lamulungu pa 8 April, 2012.

P.O Box 44, Florida 1710, South Africa•Tel:+27-11-472-3615•Fax:+27-11-672-7614•E-mail:nazarene@africa-region.org.za

Kutuluka mu Pasaka kulowa mu Pentekose, 8 April – 27 May 2012, mpingo udzapitilira mukusanthula Mawu ndi kukhala ndi nthawi yolowa mchiyero cha wekha komanso gulu mosatira dongosolo la Wesley ndi cholinga choti onse otengapo gawo pa utumiki umenewu alowe kapena kukonzanso pangano la ubale wawo ndi Mulungu ndi Mpingo.

Cholinga chofunikira kwambiri pa dongosolo limeneli ndi chakuti tikhale zida za mpingo "zofuna chiyanjano choyera Chachikhristu, kutembenuza mtima ochimwa, chiyeretso chathunthu cha okhulupirira, kuwathandiza kukula m'chiyero chawo, ndi kukula mu mphamvu za uzimu mosavuta monga zikupezekera m'Chipangano cha Mpingo Watsopano" (Buku La Malamulo Ndi *Mayendetsedwe A Mpingo Wa Nazarene 2009-2013*, ¶25).

Abusa, ndikufuna ndikupempheni inu ndi mpingo wanu mwapadera kutenga nawo gawo mu dongosolo la Chikondwerero cha Chiyero. Chonde onetsesani mosamala mabuku ndi makanema onse kuphatikizapo paketi iyi kapena amene mudzalandire mtsogolo, ndipo khalani omasuka kufunsa a field strategy coordinator anu kapena office yanga pa thandizo lililonse kapena pamene simukumvetsetsa bwino.

Zikomo potengapo gawo pa Chikondwerero cha Chiyero!

Dr Filimao Chambo
Regional Director for Africa
Church of the Nazarene

P.O Box 44, Florida 1710, South Africa•Tel:+27-11-472-3615•Fax:+27-11-672-7614•E-mail:nazarene@africa-region.org.za

Chigawo Cha Africa:

- Pali maiko 54 mu chigawo cha Africa:
  - Maiko 48 apamtunda ndi 6 ali pa zilumba
- Africa ndi chigawo chachiwiri kukula ndipo ndi chigawo chachiwiri chimene chilli ndi anthu ochuluka kwambiri:
  - 11.7 million square miles
  - Chiwerengero chokwana 1 billioni cha anthu (kaundula wa 2009)

Utumiki wa Mpingo wa Nazarene – Chiwerengero:

- Mpingo uli mu maiko 42 mwa maiko 54 mu Chigawo cha Africa
- Mpingo unayamba m'chigawo chakumpoto kwa Africa ku Cape Verde mu chaka cha 1901
- Mpingo unayamba m'chigawo cha ku mmwera kwa Africa ku Swaziland mchaka cha 1910
- Kuyambira 1901 mpaka 1950 mpingo unali m'maiko anayi okha
- Kuyambira 1950 mpaka 1980:
  - Mamembala = 37,000
  - Maiko onse amene talowamo = 9
- Kuyambira 1980 mpaka 1990:
  - Mamembala = 71,121
  - Maiko onse amene talowamo = 19
- Kuyambira 1990 mpaka 2000:
  - Mamembala = 173,690
  - Maiko onse amene talowamo = 35
- Kuyambira 2000 mpaka 2010:
  - Mamembala = 511,000
  - Maiko onse amene talowamo = 42
- Utumiki wa Mpingo wa Nazarene mu Africa ndi utumiki ongoyamba kumene:
  - 78.5 % ndi utumiki wa zaka 30 kapena kuchepera apo
  - 61% ndi utumiki wa zaka 20 kapena kuchepera apo
- Lero pali zigawo 125 zimene zapanga zigawo zazikulu zisanu ndi ziwiri motere:
  - Central
  - East
  - Horn
  - Lusophone
  - Middle
  - South
  - West
- Ndipo pali:
  - Mipingo 4,237 yokhazikika ndi mipingo 4,195 yomwe abusa amachita kuyendera
  - Tiri ndi Abusa pafupifupi 4,000 aphunzitsidwa m'chigawochi
  - Ophunzira oposa 6,750 ku sukulu za Nazarene kukonzekera kuti akhale abusa

Mamembala oposa 549,000

CELEBRATING HOLINESS

CHURCH OF THE NAZARENE-AFRICA REGION

2012 KANEMA & MABUKU

KUPEMPHERA & KUSALA KUDYA
MATSIKU: 22 FEBRUARY – 08 APRIL

KUKONDWERERA CHIYERO
MATSIKU: 08 APRIL – 27 MAY

DZIDA ZA PEMPHERO:

- **Mmene Mungapemphere**
- **Kalendala Ya Pemphero**
- **Kuyenda Mpemphero**
- **Prayer Summit**
- **Dansi ya Pemphero ndi Matamando**
- **Ola Limene Limasintha Dziko**

VIDIYO yochokera kwa Dr Chambo
Malangizo A Masalidwe
Thandizo Pa Ulaliki
Malangizo Mmene Mungayambire Gulu Laling'ono
Mapemphero A Mbanja
Kuwerenga Mau:
Ana ang'ono, Ana ukulirapo, Achinyamata, Akulu

MABUKU OLEMBEDWA MU:

- ***Amharic***
- ***Chichewa***
- ***English***
- ***French***
- ***Malagasy***
- ***Portuguese***
- ***Shangaan***
- ***SiSwati***
- ***Swahili***
- ***Spanish***

PA MAKINA A COMPUTER:
www.africanazarene.org

P.O Box 44, Florida 1710, South Africa•Tel:+27-11-472-3615•Fax:+27-11-672-7614•E-mail:nazarene@africa-region.org.za